UNDUNA WA ZACHILENGWE

# KUKONZEKERA NYENGO YA EL NINO

*June 2026*

## Mawu Oyambilira

Kauniuni wa zanyengo waonetsa kuti dzinja la chaka chino ikuyembekezeka kukhudziwa ndi El nino ndipo zikuonetsa kuti El nino yu akhala akukhudza nyengo mpaka kulowa chaka cha mawa cha 2027. Ulosi wa zanyengo ukuonetsa kuti pali kuthekera kwakulu kokhala ndi El nino wamphamvu kwambiri,ngakhale kuti El nino yu sakuyembekezerekera kuposa mphamvu ya El nino wa chaka cha 2025/2016 yemwe ndi El nino wa mphamvu kwambiri kuchokera mchaka cha 1982.

Ku Malawi kuno, zikutanthauza kuti pali chiopsezo chachikulu chokhala ndi mvula yochepa makamaka m'madera ambiri a kum'mwera mu miyezi ya October mpaka December yomwe alimi amakhala akudzala mbewu. Palinso chiopsezo chachikulu cha ng'amba maka miyezi ya pakati pa January ndi March 2027. Komabe, pali kuthekera kuti madera ambiri a kumpoto ndi ena a pakati angalandire mvula ya mlingo okhazikika kapena kuposera mlingo okhazikika miyezi ya pakati pa October ndi December.

Choncho, pakufunika kuti boma komanso mabungwe osiyanasiyana athe kugwilana manja pofuna kuthandizira anthu kuti akhale ndi chakudya, madzi aukhondo komanso moyo wathanzi.

## Ulosi Woyambirira Wa Dzinja Mwachidule

| Mlozo | Ulosi wa nyengo ya dzinja |
|---|---|
| **Mlingo wa El Niño** | El nino wa mphamvu kwambiri |
| **Mlingo wa mvula mu miyezi ya October-December** | Mvula yochepa makamaka madera ambiri a kumwera makamaka mu mwezi wa December. |
| **Ng'amba mu miyezi ya January-March** | Mvula yogwa masiku ochepa, komanso kuthekera kwakulu kokhala ndi mvula yochepera mlingo okhazikika |
| **Mlingo wa Madzi mu Nyanja ya Malawi** | Kutsika kwa mlingo wa madzi mu nyanja ya Malawi. |
| **Kuyelekeza zotsatira za El nino wa chaka chino ndi mbuyomu Zaka 2015/16 ndi 2023/24** | Anthu ambiri oposa 2.8 million anakhudziwa mu 2015/2016 ndipo 4.2 million anakhudziwa mu 2023/24 pakusowa chakudya |

## M'mene El Nino Angakhudzile Chitukuko Ndi Zoyenera Kuchita

| Gawo | Chiopsezo | Zomwe tingachite |
|---|---|---|
| **Ulimi** | Kuchedwa kwa mvula, ng'amba Kapena chilala madera ambiri kum'mwera | ● Kudzala mbewu zopilira ku ng'amba/chilala<br>● Kudzala mbewu zocha msanga |

| | | |
|---|---|---|
| | kuchitisa zokolora zichepe komanso chakudya chisowe | ● Kutsatira njira za ulimi wa makono otsatira nyengo<br>● Kulimbikitsa ma uthenga othandiza alimi<br>● Kuchitira ulimi wa m'nthilira |
| **Ntchito zokhudza madzi** | Mlingo wa Madzi mu Nyanja ukuyembekerekera kutsika pang'ono ndi 0.2–0.7 m zomwe zingakhudze ulimi wa mthilira komanso ntchito zopereka madzi kwa anthu mu zaka ziwiri zikubwerazi | ● Kulimbikitsa ntchito zosamalira madzi<br>● Kuteteza madera omwe amasunga madzi<br>● Kuteteza katundu osamalira madzi |
| **Ntchito zokhudza Umoyo** | Chipsyezo cha kuchuluka kwa matenda osiyanasiyana odza chifukwa cha nyengo monga cholera | ● Kulimbikitsa ntchito za umoyo ndi ukhondo<br>● Kukonzekeletsa zipatala kuti zikhale ndi zipangiso komanso ogwira ntchito okwanira<br>● Kuchita kampeni odziwitsa anthu kufunika kwa ukhondo |
| **Ngozi zogwa mwadzidzi** | Kusowa kwa chakudya anthu ambiri | ● Kukonza ndondomeko zokonzekera Ngozi zogwa mwadzidzi<br>● Kulimbikitsa ntchito zopereka machenjezo a zanyengo<br>● Kukonzekera katundu/zinthu zothandizira Ngozi zogwa mwadzidzi |

## Zomwe Adindo Angachite

**Unduna Wa Zachilengwe Kudzera ku Nthambi Ya Zanyengo Ndi Kusintha Kwa Nyengo**: kuunika nyengo ya El Nino, kupereka ulosi komanso machenjezo osiyanasiyana, ndi kuthandiza mabungwe ndi nthambi zina za boma

**Nthambi Yoona Zangozi Zogwa Mwadzidzi**: Kulumikizitsa mabungwe ndi nthambi za boma pa ntchito yokonzekera komanso kuthandiza pa Ngozi zogwa mwadzidzi.

**Ma Unduna a boma**: Kukhazikitsa ndondomeko komanso ma plan awo moganizila nyengo, kulimbikitsa ntchito yokonzekera Ngozi zogwa mwadzidzi

**Ma boma ang'ono ang'ono**: Kulumikizitsa magulu osiyanasiyana kukonzekera Ngozi zogwa mwadzidzi komanso kulimbikitsa ndi kuthandiza kupereka machenjezo a zanyengo

**Ma bungwe othandiza dziko pa chitukuko**: kuthandiza ntchito zothana ndikusintha kwa nyengo komanso kukonzekera Ngozi zogwa mwadzidzi

**Anthu a Kumudzi:** Kutsatira malangizo okonzekera othandiza kuchepetsa mavuto obwera chifukwa cha nyengo. Kutsatira mwachidwi mauthenga ndi machenjezo a zanyengo

## Zoyenera Kuchita Pakanali Pano

- Kukhazikitsa magulu a boma okonzekera nyengo ya El Nino
- Kuchita kauniuni wa zosowekera mu ntchito zosiyanasiyana
- Kupereka mauthenga ndi ulosi wa El Nino

- Kuchita kampeni yodziwitsa ndikuphunzitsa anthu
- Kukonzanso ndondomeko zokonsekera Ngozi zogwa mwadzidzi

## Ndondomeko za ku Unduna Wa Zachilengwe

Unduna Wa Zachilengwe uchita zina ngati:

- **Kupereka Machenjezo:** Kupereka ulosi wa za nyengo wa dzinja ofikira mpaka pa boma.
- **Kupereka machenjezo kudzera mu njira zamakono:** Kupereka mauthenga ofikira anthu onse kuphatikizapo aku mudzi, komanso mu chilankhulo chakuderalo kudzera pa SMS ndi mayilesi akumudzi.
- **Ma unduna a boma:** Kulimbikitsa mgwirizano pakati pa maunduna osiyanasiyana monga wa za ulimi, wa zamadzi pofuna kuthandiza kupereka uthenga othandiza magawo osiyanasiyana monga ntchito za alimi ang'ono ang'ono.





**Figure 1: Mapu kuonesa ulosi wa mvula miyezi ya October, November ndi December**

**Dziwani:**
***Ulosi wa mvula omwe waperekedwawu pakanali pano ndi ongopenekera chabe. Ulosi weni weni okhazikika uperekedwa posachedwapa nyengo ya dzinja lisanayambe***

**For further information, contact:**
The Ministry of Natural Resources through the Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, P. O. Box 1808, Blantyre
Tel: (265) 882 266 579 Email: metdept@metmalawi.gov.mw Web: www.metmalawi.gov.mw
**Facebook:** Department of Climate Change and Meteorological Services **WhatsApp**: +265 991 690 061
For area specific forecast, download: **Zanyengo App on play store**